# KALAMBULA BWALO

# NDI

# NDONDOMEKO

# ZA

# KAYENDETSEDWE KA MAPHUNZIRO

**Harvestime International Institute**

## ZA MKATIMU

Zamkatimu…………………………………………………………………………………...2
Mau Oyamba…………………………………………………………………………………3
Zolinga………………………………………………………………………………………3

### GAWO 1: MAPHUNZIRO OYAMBA

Harvestime International Network:
Dzina…………………………………………………………………………………………4
Mau a Cholinga…………………………………………………………...…………………6
Chiphunzitso Chathu…………………………………………………………..……………7

Harvestime International Institute:
Dzina………………………………………………………………………….…………….11
Zimene Sitiri ………………………………………………………….……………………11
Magawo ndi Ntchito Zake …………………………………………………………………12
Pamene Maphunziro Anakhazikika Kwambiri ……………………………………….14
Kukhala Wopindula Muuzimu ……………………………………………….………..……15
Kupita Chitsogolo ……………………………………………………….…………………16
Ogwira ntchito ku Insitute ……………………………………………….…………..….16
Othandizira kukonza M'ndandanda wa Maphunziro ………………………..……………16
Ndandanda wa maphunziro ……………………………………………………………..….17

### GAWO 2: MLOZO OPHUNZIRA PA OKHA

Kayalidwe ka Maphunziro ………………………………………………………………….22
Zipangizo Zophunzirira …………………………….……………………………………….23
Ndondomeko Zisanu ndi Ziwiri Zophunzirira …………………………...…………………23
Kuphunzira pa Ngongole ……………………………………………………………………...24
Kaundula wa Mwana wa Sukulu …………………………………………………………..….25

### GAWO 3: MLOZO WA MAYANG'ANIRIDWE A ZINTHU

Nchito: Kuphunzitsa Anthu Wamba ………………………………………….………26
Maluso Omuyenereza Munthu ……………………………………………………….….28
Maphunziro ophunzitsira anthu …………………………………………………………….28
Kukhazikitsa Masukulu Okhazikika ………………………………………………….…….28
Kusungidwe ka Kaundula wa Zinthu ……………………………………...………………28
Kuphunzira M'magulu: Kukonzekereratu ……………………………………………………29
Kuphunzira m'magulu: Kupangitsa Maphunziro ……………………………………..…….31
Malamulo a Kumasulira ndi Kusindikiza Mabuku ………………………………….....….33
Chidziwitso Chosindikizira Mabuku ena Ambiri ……………………………………… .34
Chidziwitso Chomasulira ………………………………………………………………...35

## MAU OYAMBA

Buku la Mau Oyamba liri ndi mapahunziro oyamba ndi mlozo wa kayang'aniridwe ka zinthu zokhudzana ndi Harvestime International Institute, nthambi yoyang'anira maphunziro ku Harvestime International Institute.

Gawo loyamba la bukuli limapereka Mau Oyamba a utumiki wa Harvetime International Network ndi Insititute.

Gawo lachiwiri liri ndi ndondomeko ya zipangizo za maphunziro a ophunzira pa okha.

Gawo la chitatu ndi mlozo umene umapereka ndandanda wa maphunziro a m'magulu, kusindikiza mabuku ndi kumasulira m'ndandanda wa maphunziro.

**ZOLINGA**

Maphunziro oyamba ndi mlozo wa kayang'aniridwe ka zinthu.

- Kutiwonetsa za utumiki wa Harvestime International Network and Institute. □ Kupereka chithunzithunzi cha zolinga za maphunziro.
- Kupereka ndondomeko za maphunziro a ophunzira m'magulu.
- Kufotokoza za kusindikiza mabuku, magawidwe ndi malamulo omasulira malamulo.

**GAWO 1**
**KUPEREKA CHITHUNZITHUNZI CHA HARVESTIME**

Harvestime International Network: Dzina la bungwe limapereka chinthunzithunzi cha cholinga:

**Harvestime:**

M'mene mauwa anapangidwira amatsindika kuti lamulo la Yesu likuyenera kuchitidwa mwa changu. Baibulo limanena kuti "Pamene palibe masomphenya anthu amawonongeka" (Miyambo 29:18). Yesu Khristu analamulira akuphunzira ake ndi amodzi mwa masophenya akulu kwambiri mthawi yonse:

> **"….. Kodi simunena inu kuti yatsala miyezi inai ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta" (Yohane 4:35).**

Mavuto a wogwira ntchito m'khololola la uzimu pa dziko lapansi amachuluka tikamayandikira kubweranso kwa Ambuye ndi mphulumutsi wanthu, Yesu Khristu.

Kumbali ya dziko lapansi, kukolola ndi njira yobweretsa pamodzi mbeu zimene zinapsya, kupindulapo pa ntchito iriyonse imene anthu anagwira.

Kumbali ya uzimu mfundo ya ku dziko lapansi ya kukolola imakhudzana ndi kukhwima kwa miyoyo ya amuna, akazi ndi ana polalikira uthenga wabwino.

Yesu anati:

> **……… Pomwepo ananena kwa ophunzira ake, zotuta zichulukadi koma antchito ali owerengeka (Mateyu 9:37)**

Njira yokhayo imene khololola la Uzimu limakhwimira ndiyakuti m'khristu aliyense azichitapo kanthu akawona m'mene malo akhololola aliri.

Chifukwa cha maso mphenya amenewa, Harvest International Network ndi odzipereka kudzutsa mtundu wa ogwira ntchito pa dziko lonse lapansi kuti akagwire ntchito ku khololola la uzimu.

**DZIKO LONSE LAPANSI:**

Mau akuti "padziko lonse lapansi" atanthawuza pakati pa mitundu. Masomphenya anthu ndi adziko lonse ndipo amaima kwambiri pa magulu a anthu amene asanafikilidwe ndi Uthenga Wabwino.

**KULUMIKIZANA:**

Uku ndi kubwera pamodzi kwa zinthu zimene zimapanga thunthu. Kugwira ntchito pakati pa mipingo, mabungwe ndi mitundu polumikizana kumbali ya kufalitsa ndiwo maso mphenya a utumiki umenewu.

Kunena mwa chidule, kulumikizana kumakhudzana ndi anthu kulankhulana, kugawana maganizo, uthenga ndi zofunika kuti akwaniritse cholinga chimodzi. Kumbali ya Harvestime International Network, cholingachi ndi kufikira dziko lonse lapansi ndi uthenga wabwinno.

Kulumikizana kungafanizidwe ndi maukonde asomba amene maso ake amakhala amilingo yosiyanasiyana koma amakhala ofanana m'njira zambiri.

Tanthawuzo la chipangano chatspano la mpingo ndi chitsanzo cha kulumikizana. Dziko limafanizidwa ndi thupi lokhala nazo ziwalo zambiri. Okhulupirira amene ali ndi mphatso zosiyanasiyana amagwira nchito pamodzi kuti akwaniritse cholinga chimodzi (1 Akorinto 12:4 31).

Mau a Mulungu ndi utsogoleri wa Yesu Khristu ndiyo mphamvu imene imabweretsa pamodzi.

## MAU A CHOLINGA

Yesu Khristu analunjikitsa chidwi cha ophunzira pa kholola la Uzimu la dziko la pansi:

> **Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu kwezani maso anu nimuyan'gane m'minda kuti mwayenera kale kufikira kumweta. (Yohane 4:35)**

Nkhawa imene Ambuye anatipatsa ndi ya ogwira ntchito, amuna andi akazi amene amadziwa kukolola m'kholola la uzimu pa dziko lapansi, kupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu, ndi kubweretsa pamodzi gulu la okolola a padziko lonse lapansi amene akhoza kukwanitsa ku:

1. Kupembedzera okolola a padziko lonse lapansi:

   **Pomwepo ananena kwa ophunzira ache, zotuta zichulukadi koma anthito ali owerengeka. Chifukwa chake pempherani mwini zotuta kuti akokose antchito kukututa kwache. (John 4:35)**

2. Malankhulidwe a mfundo zakholola la Uzimu.

   **Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)**

3. Chiwonetsero cha mfundo za kholola la Uzimu;

   **Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa anzeru, koma m'chionetso cha Mzimu ndi cha mphavu: (1 Akolinto 2:4-5)**

4. Kulumikizana pa kufunika kwa lamulo lokhudzana ndi kholola la uzimu pa dziko lonse lapansi:

   **Masika apita mphakasa yatha ndipo ife sitinapulumutsidwe (Yeremiya 8:20)**

5. Kubweretsa pamodzi okhulupirira mthupi la Khristu kuti akakolole malo okhazikika pa dziko lonse lapansi, ku kholola la masiku otsiriza:

   **…………M'nyengo yache atisungira ife msabata olamulidwa a masika. (Yeeremiya 5:24)**

## CHIPHUNZITSO CHATHU

Masomphenya ndi cholinga cha Harvestime International Network chakhazikika pa mfundo za uzimu za kukolola zimene zawonetsedwa m'mau a Mulungu. Mau a chimphunzitso a bungweli akhazikikanso pa masophenyawa:

## MAU A MULUNGU

Mbewu

Mbewu ndi Mau a Mulungu….. (Luka 8:11)

Malembo a m'chipangano chakale ndi chatsopano ndi mau owona a Mulungu, maziko a chikhulupiriro cha chikhristu, ozindikiritsa, moyo ndi utumiki. Malemba alibe zolakwika ndipo sikololedwa kuonjezerapo, kuchotserapo, kapena kusinthidwa ndi zikhalidwe kapena vumbulutso lililonse.

Mau anu aikika kumwamba kosatha Yehova (Masalimo 119:89)

## MULUNGU M'MODZI MWA ATATU

**Mbuye wa Kholola**

Chifukwa chache pempherani mwini zotuta kuti akokose antchito kukututa kwache. (Mateyu 9:38)

Pali Mulungu Tate, Mulungu mwana, Yesu Khristu, ndi Mulungu Mzimu;

Pakuti pali atatu akuchita umboni, Mzimu, ndi madzi, ndi mwazi ndipo iwo atatu ali m'modzi.

### MULUNGU TATE:

Pali Mulungu m'modzi, wopanda malire, wamuyaya ndi wangwiro, amene analenga zakumwamba ndi zapansi:

> **Pakuti atero Yehova amene analenga kumwamba iye ndiye Mulungu amene anaumba dziko lapansi, nalipanga Iye analikhazikitsa sanalilenge mwachabe Iye analiumba akhalemo anthu Ine ndine yehova ndipo palibe wina. (Yesaya 45:18)**

### MULUNGU MWANA, YESU KHRISTU:

Yesu anabadwa kwa Mariya, namwaliyo amene anaima mwa mphamvu ya mzimu woyera. Anali mphatso yamgwiro ya tchimo la dziko lonse lapansi kudzera mu imfa yake ndi kukhetsedwa kwa mwazi wake.

Anauka kwa akufa m'thupi lake la ulemerero, nawonekera kwa ambiri nakwera kumbwamba ndipo adzabweranso pa dizko lapansi mwa mphavu ndi ulemelerero. Ndipo tsopano ndi mutu wa thupi, mpingo wopambana mphavu zonse za satana ndipo ali kudzanja lamanja la Mulungu kumene akupembedzera oyera nthima onse.

> **Mwa ichinso Mulungu anamkwezetsa iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse, kuti mdzina la Yesu bondo lirilonse lipinde, la za m'mwamba ndi za padziko ndi za pansi pa dziko, ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Khritu ali Ambuye, kuchitira ulemu Mulungu Atate. (Afilipi 2:9-11)**

**MULUNGU MZIMU:**

Mzimu woyera unawuzira mpweya pa mau a Mulungu, unadzoza Yesu Khritu pa utumiki wake, unadzadza mpingo ndi mphavu ya pentekoste, ndipo udzasitha matupi a okhulupirira kukhala matupi a wulemelero pa kuwuka kwa akufa.

Mzimu woyera amatsuta dziko za uchimo, chilungamo ndi chiweruzo, kuyanjanitsa muthu ndi Yesu Khritu ndipo umazindikirika ndi kuthekera kokhala mboni yamphavu ya chiwukitso cha Ambuye komanso kutsimikizika ndi zodabwitsa komanso zozizwa Machitidwe 2:4.

> **Komatu mudzalandira mphavu, Mzimu woyera atadza painu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samaliya, ndi kufikira malekezero ache a dziko. (Machitidwe 1:8)**

Mphatso za mzimu zimaperekedwa kwa okhulupirira kudzera ku utumiki wa Mzimu woyera. Umene unapereka kwa muthu aliyesne monga afuna:

> **Koma zonse izi achita mzimu mmodzi yemweyo, nagawira yense payekha monga afuna (1 Akolinto 12:11).**

Mzimu Woyera amaperekanso chipatso, kupereka kuthekera kwa okhulupiria kuti akule mchiyeretso:

> **Koma chipatso cha Mzimu ndicho Chikondi, chimwemwe, mtedere, kuleza mtima, chifundo kukoma mtima, chikhulpiriro, chifatso, Chiletso, pokana zimenezi palibe lamulo. (Agalatiya 5:22-23)**

## MUNTHU

### Ofesa

**Verani taonani wofesa anaturuka kukafesa; (Marko 4:3)**

Munthu analengedwa mchifanizo ndi mchikhalidwe cha Mulungu. Kudzera ku tchimo loyamba

Adamu ndi Heva, anthu onse anakhalanso ochimwa. Muthu alibe mphavu yobwrera kwa Mulungu pa iye yekha, ndipo ndi otayika opanda chiyembekezo cha chipulumutso cha Yesu Khristu.

> Koteronso kwalembedwa, Munthu woyamba, Adamu anakhala mzimu wamoyo, Adamu wotsirizayo anakhala mzimu wakulenga moyo. Koma chauzimu sichiri choyamba koma chachibadwidwe: pamanepo chauzimu. Muthu woyambayo ali wapansi, wathaka Munthu wahiwiri ali wakumwamba. (1 Akolinto 15:45-47)

## CHIPULUMUTSO

### Kholola

Ndipo iye amanena afesedwa pa nthaka yabwino , uyu ndiye wakumva mau nawadziwitsa; amene abaladi zipastso, (Mateyu 13:23)

Chipulumutso ndi mphatso ya Mulungu kudzera ku chisomo ndi chikhulupiriro mwa Yesu Khristu. Palibe dzina kupatulapo la Khristu limene anthu akhoza kupulumutsidwa nalo.

Pakusiya tchimo, kubereka zipatso za kulapa, ndi kukhulupirira Yesu Khristu ndi imfa yake pa machimo a onse, munthu amabadwanso mwatsopano kukhala ndi moyo wosatha mwa mzimu woyera.

Kudzera ku chiwombolo chimenechi chikhulululukiro cha machimo, kumasulidwa ku nsinga ya dziko, ndi ufulu mwa mzimu wa Mulungu.

> Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakucita mwa chikhulupiriro ndipo ichi chosachokera kwa inu: chiri mphatso ya Mulungu; chosachokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyesne. (Aefeso 2:8-9)

## MPINGO

### Ogwira Ntchito

Chifukwa chache pempherani mwini zotuta kuti akokose antchito kukututa kwache (Mateyu 9:38)

Mpingo ndi thupi komanso kwatibwi wa Yesu Khristu. Ntchito yoyambirira ya Mpingo ndi kuphunzitsa anthu a mitundu yonse, kutengera uthenga wabwino wa Ufumu kwa anthu amitundu yonse ndi zitsimikizo za zodabwitsa:

> Ndipo ananena nao, Mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani uthenga wabwino kwa olengedwa onse. Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalangidwa.  Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira;

> m’dzina langa adzatulrutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako sikadzawapweteka adzaika manja pa odwala ndipo adzachira. (Marko 16:15-18).

## CHIMALIZIRO

### Kholola lo Tsiriza

Tumiza zenga lako ndi kumweta, pakuti yafika nthawi yakumweta; popeza dzinthu za dziko zachetsa. (Chivumbulutso 14:15)

Chimaliziro cha zinthu zonse chikuphatikizirapo kubweranso kwa Yesu Khristu kumene kudzakhala kwa ulemerero ndi kowoneka. Chiwukitso cha akufa, ndi kusinthidwa kwa iwo amene adzakhala ali mwa Khristu ku chiweluzo cha olungama ndi osalungama. Satana ndi khamu lake ndi anthu onse amene ali kunja kwa Khristu adzalekanitsidwa pamanso pa Mulungu kukakumana ndi chilango pamene owombolodwa adzakhala ndi Mulungu kwa muyaya:

> Koma sitifuna abale kuti mukhale osadziwa za iwo akugona; kuti mungalire monganso otsalawo, amene alibe chiyembekezo. Pakuti ngati tikhulupirira kuti Yesu adamwalira nauka, koteronso Mulungu adzatenga pamodzi ndi iyewo akugona mwa Yesu. Pakuti ichi tinena kwa inu m’mau a Ambuye, kuti ife okhala ndi moyo, otsatira kufikira kufikanso kwa Ambuye, sitidzatsogolera ogonawo. Pakuti ambuye adzatsika kumwamba mwini yekha ndi mfuwu ndi mau a m’ngwelo wamkuru ndi Lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuwuka; pamenepo ife okhala ndi moyo otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m’mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. (1 Atesalonika 4:13-17)

> Ndipo ndinaona akufa, akuru ndi ang’ono alinkuima ku mpando wachifumu; ndipo mabuku anatsegulidwa; ndipo buku lina linatsegulidwa, ndilo la moyo ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m’mabuku monga mwa ntchito zao (Chivumbulutso 20:12)

## HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

### DZINA

Mau akuti “insitute” osati malo ophunzirira kapena sukulu anasankhidwa chifukwa dzina lopangidwa kuchokera ku liwu limeneli kupatula malo ophunzia limatanthawuzanso umodzi kapena gulu la anthu obwera pamodzi. Izi zikupereka chithunzithunzi cha mbali ya utumikiwu maka kumbali ya kulumikizana, kuthandiza mabungwe pophunzitsa anthu wamba.

Mau akuti “institute” ngati mneni amatanthawuza kuti “kukhazikitsa, kukulitsa, kupanga, kuyambitsa, ndi kupangitsa masophenya, Insitute ikubala masomphenya opangitsa anthu wamba kuti asangokhala ndi masophenya chabe koma kuti akwaniritse, komanso kuti asangokhala owonerera ndi kuwonetsera mphavu ya Mulungu.

### ZIMENE IFE SITIRI

Harvestime Intenertional Institute si sukulu yophunzitsa za amene akufuna kuphunzira zinthu za mau a Mulungu monga zilankhulo za Baibulo, mbiri, zofufuza-fufuza ndi zina.

Harvestime Institute sili pa mpikisano ndi ma sukulu a mau a Mulungu. Kwa amene maphunziro komanso chuma chingawalole  ali ndi kuthekera kopita ku sukulu zimenezi, ndipo pali ena amene zocitika sizingawalole, timalimbikitsa maphunziro a mau a Mulungu. Maphunziro anthu ndi anthu wamba amuna ndi akazi amene alibe mwayi wa maphunziro ngati amenewa.

Bungwe limene limathandiza, Harvestime International Network, si mpingo, ndipo silimafunanso kukhazitsa dongosolo la mpingo. Ndi ngwirizano wa anthu ogwira ntchito ndi mipingo, mabungwe, ndi mitundu podzutsa ogwira ntchito ku kholola limene liri ku dziko.

Maphunzirowa si ndandanda wa zochitika zongodzithandiza okha. Mulungu sakuphunzitsa anthu ongodzikonzanso okha koma amatenga akufa, amuna ndi akazi ndikuwapanga kukhala amoyo mumzimu. Izi ndi zosiyana kwambiri ndi kudzithandiza wekha.

## MAGAWO NDI NTCHITO ZAKE

Harvestime Institute ndi mamphunziro amene ankhazikitsida kuti afikire mbali ina iriyonse ya thupi la khritu. Maphunziro amenewa amakhazikika pa mau a Mulungu ndipo atha kugwiritsidwa ntchito ndi amene angafune kuphunzira mau paokha, pagulu, m'manyumba, pa bungwe, *sukulu, ndende, m'mipingo ndi m'maiko ambiri pa dziko lonse.*

Harvestime International Insitute inakhazikitsidwa chifukwa cha mzimu woyera ndipo ndi yankho la mfuwu wochokela ku malo a kholola pa zofunika pophunzitsa anthu wamba. Amphunzitsi amene amaphunzitsa athu wamba amapeza kuti maphunzirowa ndiopidula m'jira ziwiri izi;

Choyambirira pali maphunziro a mau a Mulungu amene amaphatikiza zilankhulo monga Latini, Griki, Zofufuza- fufuza ndi maphunziro ena ambiri sanamphatikizidwe m'nthawi imene ophunzira amaphunzitsidwa ndi Yesu Khristu. Maphunziro ambiri a chonchi ndi ovuta kuti anthu wamba awavetsetse. Malo amene ma sukuluwa ali ndi mitengo ya ndalama zoyenera kulipira ndizovuta kuzikwanirita.

Chachiwiri njira imene ma sukulu amatsata singakwanitse kupanga kuti anthu wamba asinthe kuchoka pakukhala ndi masophenya chabe kufikila pa kukwaniritsa. Chitsanzo;

> M'masukulu ena ophunzira amphunzitsidwa kuti angakhale bwanji ndi mphavu ya Mulungu pokhazikika kwambiri pa zodabwitsa, koma maphunziro saperekedwa pa zochitika zeni zeni za moyo wa tsiku ndi tsiku. Amatha kuphatikiza ndi changu koma osadziwa kuti angagwiritse banji ntchito mphavuyo.
>
> Ma sukulu ena amatsindika kwambiri "kukhala nkhrsitu wopambana" pamene zoyambirira za chikhulupiriro zimasalidwa. Anthu ena amaphunzitsidwa kukhala ndi moyo wachipambano koma samavetsetesa bwinobwino kuti kubadwa mwatsopano kutanthawuzanji.
>
> Ma sukulu ena, ophunzira amawuzidwa mavumbulutso akuya a Mulungu amene amawalimbikitsa, koma samawuzidwa kuti atha kuwerenga bwanji mawu a Mulungu kuti alandire mavumbulutso awo kudzera mwa Mzimu Woyera. Amangotengera zimene amva.

Harvestime International Institute siri ndi mitengo yokwera kwambiri kusiyana ndi sukulu zophunzitsira mau a Mulungu maka kumbali ya maphunzitsidwe ake ndi zimene zimaphunzitsidwa. Komanso sizimakhala ndi china chirichonse monga sukulu za mau a Mulungu chifukwa amachotsa zipangizo zimene sizikhudzana kwambiri ndi kukula m'moyo wa uzimu komanso kukhala opindulitsa.

Maphunzizrowa samachitikira mbali imodzi. Kuchokera pa intaneti, zipangizo zosungila uthenga mu computer, fulashi, malo a inteneti, malo omasulira mdera lanu, malo osindikiza mabuku,

maphunzirowa atha kuchitika pena paliponse pa dziko lapansi zimene zimapangitsa kuti anthu wamba kuti aphunzitsidwe posasiya malo amene akukhala panopa. Maphunziro amachitika mokhudzana ndi chikhalidwe chawo, powona zochitika zawo za tsiku ndi tsiku kukhala zosasintha komanso akukhala malo amene azikwanitsa kuchita zimene akuphunzira. Maphunzirowa amagwiritsa ntchito nthawi ngati chinthu chabwino chothandiza kuti amphunzire modziyimira paokha. Cholinga cha maphunziro sikupanga anthu kuti asamadzidalire, koma kuti azidzidalira okha.

Insitutue simagwiritsa ntchito ndalama zambiri pomanga malo ophunizira. Maphunziro atha kuchitikira mzipinda zimene ziripo kale, kaya ndi kunyumba, ku church, school, Yesu sanamange zipinda komabe utumiki wake unathandiza anthu kukwaniritsa masophenya. Maphunziro amakhala amphavu ya Uzimu ya Mulungu chifukwa cha zimene zikuphunzitsidwa osati chifukwa cha zipinda zimene anthu akuphunziriramo.

Mtsogoleri wamphamvu mdziko la Amerika, Benjamini Franklin, anati, “Ndipatsent atsogoleri 26 ankhondo ndipo ndigonjetsa dziko lapansi” amatanthawuza ntundu wa makina osindikizira mabuku okhala ndi zilembo 26 m’chilankhula cha chingelezi. Amazindikira mphavu ya masamba osindikizidwa. Magawidwe ndi mamasulidwe a mau olembedwa a Mulungu, Baibulo, limawonetsa kupambana kwa njira imeneyi yolumikizirana ndi anthu.

Zikomo chifukwa cha chitukuko, Harvestime International Institute itha kufikira maiko ambiri opanda kulipira ndalama zambiri m’malo ofikira Katundu ndi kulowera alendo. Imatha kupezeka pa tsamba la intaneti posalipira kena kalikonse padziko lapansi. Zipangizo zophunzirira zimapangidwa m’maiko ambiri pogwiritsa ntchito ndalama zochepa zimene ngakhale anthu wamba atha kukwanitsa.

Institute si maphunziro a kolesipondansi. Sukulu zimenezi ndizabwino pokhapokhapo pali ndondomeko zabwino zotumizira makalata. Pepeza maphunzirowa amafuna anthu ovuta kufikirika, maphunziro a kolesipondansi sangagwire chifukwa cha kuvuta kwa njira zotumizira makalata m’madera amenewa.

Insitutue ndi dongosolo limene anthu ndiwo a makhala ndi mphavu. Izi zimatanthawuza kuti likulu limakhala ndi ntchito yoyang’anira zinthu zochepa. Timapereka ndandanda wa maphunziro ndi dongosolo la kasindikizidwe, kamasulidwe ndi kaikidwe ka maphunziro, koma sitimayang’anira kachitidwe ka zinthu pa malo ophunzirira. Kupereka mphavu kwa anthu kumapangitsa kuti makulidwe achitike mwachangu ndikulola kuti maphunziro achitike mokhudzananso ndi chikhalidwe dela limene maphunziro akuchitikira.

Sukulu iriyonse imachitika payokha imasunga kaundula wake wa zinthu, ndikupereka mapepala a diploma.

Maphunziro onse a Harvestime atha kupezeka pa tsamba la intenate http: //www.harvestime.org

## PAMENE M’NDANDANDA WAMAPHUNZIRO UNAIMA KWAMBIRI

M’ndandanda wa maphunziro aku Harvesti International Institute Unaima kwambiri pa zinthu ziwiri;

**Choyamba:** Yesu anaphunzitsa ndi mau komanso chiwonetsero podzutsa atsogolereli ophunzira, ndi olimbikitsidwa. Maphunziro anaima pa zimene anaphunzitsa pakusintha anthu wamba kukhala anthu amene analalikira uthenga wabwino powonetsera mphavu yake. Nthawi zambiri timatsindika pa njira yophunzitsira ya Yesu Khristu osalabadira zimene Yesu amaphunzitsa. Koma kodi anaphunzitsa chani chimene anasitha nacho asodzi ndi amisonkho kukhala anthu okolola padziko lonse?

**Chachiwiri:** Maphunziro anaima kwambiri pa zimene zinawonetsedawa ndi kuphunzitsidwa nthawi ya Machitidwe Atumwi ndi Makalata monga dongosolo lake linakhazikika mumpingo oyambirira.

Njira iyi sikunyazitsa ubwino ndi mphavu ya malembo. Kawirikawiri Yesu anagwiritsa ntchito chipangano chakale pamene amaphunzitsa. Moyo wake ndipo maphunziro ake anaima kwambiri pa vumbulutso la mau a Mulungu. Insitute imakonzekeretsa ndi njira za kaphunzilidwe ka mau a Mululngu ndi luso limene limapangitsa kuti kuphunzira mau a Mulungu kotsatira dongosolo la maphunziro kapitirire. Timaperekananso mabuku amene amafotokoza mwachidule za mabuku ena a m’Baibulo. Komabe maphunziro a Institute amaima kwambiri pa zimene Yesu anaphunzitsa kuti anthu asakwaniritse masophenya awo chabe komanso awonetsere dongosolo limene linawonetsedwa ndikuyambitsidwa mu mpingo.

Maphunziro amatsindika chiwonetsero, kumphunzitsa anthu wamba kuti azichitapo kanthu osati akhale ongoyendayenda. Chidziwitso chabe cha Mululngu sichokwanira:

**Khalani akuchita mau, osati akumva okha, ndi kudzinyenga nokha (Yakobo 1:22)**

Chidziwitso chenicheni chimachokera ku zokumana nazo. Uthenga umakhala nawo chifukwa cha maphunziro, ochokera ku zinthu zokumana nazo. Mfundo zimaphunzitsidwa koma zokumana nazo zimathandiza kuti anthu aphunziredi ntchito. Yusu ndi munthu wamoyo osati mfundo chabe yozizira. Ubale pakati pa iye umakhazikika pa kukumana naye, osati chidziwitso chabe, mfundo ndi uthenga. Cholinga cha maphunzirowa si kungokhala ndi chidziwitso chabe koma zochitika zimene zimasintha zothekera mutumiki kukhala zowonadi. Sikungofotokoza chabe (kulankula zokhudzana ndi mphavu ya Mulungu). Koma kuwonetsera (Kuchitapo kanthu)

> **Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m’chionetso cha Mzimu ndi cha mphavu; Kuti chikhulupiriro chanu chisakhale m’zeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (1 Akolinto 2-5)**

Timakhazikika pa kuphunzira osati kuphunzitsa. Ngakhale kuti kumphunzitsa ndi mbali imodzi ya kuphunzira, kuphunzitsa kumamusiya ophunzira ndi chisankho cholandira zimene waphunzisidwa kapena kuzikana. Timakhumba kuti ophunzira;

> **………kuti adziwitse zoona zache za mau amene anaphunzira. (Luka 1:4)**

Ndongosolo la maphunzirowa limatengitsa ophunzira kuti asangokhala ophunzira chabe koma kuti asinthe, kuchokera pongokhala owonerera kufikira kukhala ochita nawo zimene ziri zofunika. Sitikungogawa chabe uthenga. Tikugawa zinthu za Mulungu kwa ophunzira.

## KUKHALA OPINDULITSA MUMZIMU

Akuphunzira akupemphedwa kuti akhale opindulita muzimu.

Pempho la khristu loyambirira kwa ophunzira ake linakhazikika pa kupindulitsa muzimu;

> **Ndipo iye ananena nao, tiyeni pambuyo panga, ndidzakusandudtani asodzi a anthu. (Matheyu 4:19)**

Lamulo lake lomalizira linali kupulumutsa anthu ambiri.

> Chifuka chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi lamwana ndi la mzimu woyera; ndi kuwamphunzitsa, asunde zinthu zonse zimene ndinakkulamulirani inu;
>
> **Ndipo onani ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansi pano. Mateyu 28: 19-20)**

Thalitchi ndi thupi la uzimu limene linatumidwa. Popeza anthu ambiri ndi anthu wamba, mphavu imeneyi ikuyenera kulimbikitsidwa kuti akhale opindulitsa kuti tikhale ndi khołola limene liri m'maiko ambiri padziko lonse lapansi. ( Onani ntchitoyi: Kuphunzitsa anthu wamba" m'gawo lachitatu la kalozera.

Mfundo za mau a Mulungu tikamazigwiritsa ntchito, maphuzirowa amapangitsa kuti okhulupirira adzutse Akhristu ena odzilimbikitsa, kupanga netweki ya kufalitsa padziko lonse lapansi. Ngakhale kuti sanaphunzitsepo kilasi ya ana, kulalikira, kapena kutumikira pakati pa anthu, okhulupirira aliyense antha kukhala mbali imodzi ya kukula kwa kulumikizana kwa gulu la kufalitssa.

Iri si dongosolo limene munthu anapanga kapena bungwe, koma dongosolo la Mulungu lovumbuluka m'malembo. Limakhazikika pa mfundo zopatsidwa ndi mtumwi Paulo kupita kwa ntumiki wang'ono otchulidwa Timoteo.

**Chifukwa cha mafumu ndi onse akuchita ulamuliro kuti m'moyo mwathu tikhale odika mtima, ndi achete m'kulemekzeza Mulungu, ndi m'klemekezezeka monse. (1 Timoteo 2:2)**

## KUPITA CHITSOGOLO

Maphunziro amphavu amene amasintha anthu kuchoka pongokhala ndi masophenya chabe kufikira pokhala ndi zinthu zenizeni, gwiritsani ntchito phunziro limene linafotokozedwa mu m'gawo la ndandanda  wa maphunziro mbukuli. Limene limadalira maphunziro ena ngakhale kuti kulola maphunzrio ena kugwiritsidwa ntchito paokha ndi chimene chimafunika. Chitsanzo m'busa atha kugwiritsa ntchito "maziko a chikhulupiriro" pa gulu la otembenuka ntima kumene posagwiritsa ntchito maphunziro ena operekedwa ndi Institute.

## OGWIRA NTCHITO KU INSTITUTE

Ndandanda wa maphunziro umalola m'busa kapena mtsogoleri wa chi khristu kuphunzitsa. Ku likulu la Harvesstime Internationa Insitutue, anthu onse olemba ndi kuwonanso bwinobwino zinthu zimene zalembedwa, omasulira, ndi onse amene amakhudzidwa samalandira malipiro pakutha pa mwezi. Ngati utumiki olumikizana, ambiri mwa iwo amakhudzidwa m'mautumiki aiwo eni ndikupereka nthawi yawo komanso maluso ku Harvestime.

## OTHANDIZIRA KUKONZA M'NDANDANDA WA MAPHUNZIRO

Anthu amene amathandiza utumiki wa Harvestime International Network kumbali yobwera ndi ndandanda wa maphunziro ndi amawudindo osiyanasiyana pakati pa akhristu (evangelical). Ena ndi amphunzitsi, atumiki, atolankhani m'malo auzimu ndi amene akugwira ntchito. Ena ali ndi ma setifikati kuchokera m'sukulu za ukachenjede. Koma sitinathere pa anthu ochokera msululu za ukachenjede zovomerezeka za mau a Mulungu. Anthu ena othandiza samawoneka koma amathandiza m'maphunziro athu wamba padziko lonse lapansi. Kuwalola anthuwa kumathandiza kuti tipewe kuti maphunzirowa akhazikike pa zochitika m'malo autumiki. Amabweretsa kaganizidwe kovomerezeka padziko lonse lapansi kuchokera ku utumiki wa m'malo autumiki. Anthu onse othandiza ali ndi zowayenereza, anabadwa mwatsopano, odzazidwa ndi mzimu, akhristu okhazikika amene amakhulupirira umulungu wa mau amene anawuziridwa ndi Mulungu. Kulumikizana ndiye chokhumba chawo pa maphunzirowa. Izi zinawabweretsa pamodzi mwa kulumikizana mwatsopano ndi cholinga chodzutsa ogwira ntchito ku khololа ladziko lonse lapansi.

## M’DANDANDA WA MAPHUNZIRO

### MAMPHUNZIRO OYAMBA NDI MLOZO WA KAYENDETSEDWE KA SUKULU

Bukuli likuwonetsa koyamba masomphenya a Harvestime International Network ndi Institute. Zolinga, dongosolo lokwaniritsira zolinga, komanso ma pangangidwe a maphunziro zafotokozedwa. Kalozera akufotokoza kuti munthu kapena gulu lingagwiritse ntchito bwino Intitute motani. Bukuli ndi chida chofunika kwa anthu kapena magulu popanga dongosolo kukhala ndi maphunziro okwanira. (ISBN#1-930703-01-5)

## *MAPHUNZIRO OYAMBA*

### BUKU LOYAMBA: KUPANGA MASOMPHENYA

Kufotokoza Masomphenya a Kholola la Uzimu.

### DONGOSOLO LA KHOLOLA LA UZIMU:

Choyambiria chimene Yesu Khritu anaitanira anthu ndi kukhala opindulitsa muzimu. “ndi tsateni ndipo ine ndidzakupangani inu kukhala asodzi a anthu”. Pamene anawalangizanso komaliza anawawuza anthu kuti akhalenso obereka zipatso za uzimu. Pogwiritsa ntchito fanizo la kholola la chilengedwe, maphunzirowa  akuima kwambiri pa malonjezano a kholola la uzimu, zinthu zimene zimalepheretsa, ndi mfungulo wa kholola labwino. Limafotokozanso za masomphenya amene maphunzirowa amakozekeretsa ophunzira kuti akwaniritse. (ISBN #1-930703-02-3).

### BUKU 2: KUKHALA OTSATIRA

**Kuphunzitsa Ogwira Ntchito kuti Akwaniritse Masophenya.**

### MAZIKO A CHIKHULUPIRIRO:

Maphunzirowa amatsindika pa ubwino wa maziko a Uzimu oyenerera a  moyo ndi utumiki pokhazikika pa maziko a chikhulupiriro cha chikhristu monga kunalembedwa pa Ahebeli  6:1: kulapa, chikhulupiriro, ubatizo, kusanjikidwa manja, chiukitso, chiweluzo.  (ISBN #1-93070303-1).

### MAKHALIDWE A MU UFUMU:

Uthenga wabwino udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi Yesu Khristu asanabwere (Mateyu 24:14). Kuvetsetsa bwino mfundo za ufumu ndi zoyenera ngati wina angafalitse uthenga wabwino wa ufumu. Phunziroli limaima kwambiri pa mfundo ndi khalidwe loyenera pa moyo ndi utumiki. (ISBN #1-9030703-04-x).

**DONGOSOLO LA UZIMU: BUKU LA NKHONDO YA UZIMU:**

Phunziroli limapanga ophunzira kudziwa modutsa dziko lapansi kufika m'zochitika muzimu. Njira za ndani zinawunikidwa ndipo dongosolo la nkhondo ya uzimu kutsimikiza chipambano mwa mphamvu ndi ulamulilo ya mziko la uzimu zafotokozedwanso.

**UTUMIKI WA MZIMU WOYERA:**

Phunziroli limayima kwambiri pa utumiki wa Mzimu woyera, zipatso za uzimu, mphatso za uzimu. Ophunzira amatsogozedwa po zindikira mphatso zao za uzimu ndi mbali yawo ya utumiki m'thupi la khristu (ISBN #1-9030703-06-6)

**KUZINDIKIRA MAU A MULUNGU:**

Phunziroli limafotokoza m'mene Mulungu amalankhulilira ndi anthu lelo komanso kuzindikira dongosolo lenileni la Mulungu pa moyo wa munthu. Chitsanzo cha kapangidwe ka chisankho ka Chikhrsitu kaperekedwanso, mogwirizan ndi ndondomeko zogonjetsera zisankho zoipa, zoyenera kuchita ngati wina wa semphana ndi cholinga cha Mulungu, ndi njira zothetsera zochitika zopereka mafuso. (ISBN #1-9030703-07-4).

**NDONDOMEKO ZA KASANTHULIDWE KA MAU A MULUNGU:**

Phunziroli limakonzekeretsa ophunzira kuphunzira mau a Mulungu paokha akamaliza maphunziro awo. Ophunzira amadziwa kawerengedwe ka mau Mulungu potsatira buku, chaputala, ndime, versi, ndi mau. Njira zina zophunzitsidwa ndi monga m'biri ya munthu, mutu, mlozo wa tsiku ndi tsiku, kagawidwe ka zinthu ndi kuvetsetsa mau a Mulungu. Zipangizo zothandiza kuvetsetsa mabuku a ndakatulo ndi uneneri zaperekedwanso ndipo ophunzira amaphunzitsidwa njira zonenera mfundo zomangirira chaputala pantima. (ISBN #1-903070308-2).

**KAFUKUFUKU WA MAU A MULUNGU:**

Kafukufuku ameneyu amapereka chithunzithunzi cha Baibulo lonse. Werengani mfundo zomangilira buku lililonse m'Baibulo, zaperekedwa kuti zithandize makulidwe a ophunzira. Gawo loyamba: Mau oyamba ndi Chipangano chakale (ISBN #1-9030703-09-0). Gawo lachiwiri: Chipangano chatsopano. (ISBN #1-9030703-10-4).

**BUKU 3: KUCHURUKANA:**
**Kuchurukitsa mphamvu ya ogwira ntchito omwe aphunzitsidwa.**

**KUPANGA MAONEDWE A ZINTHU MONGA MWA MAU A MULUNGU.**
Phunziro iri limasanthula mawonedwe azinthu monga mwa mau a Mulungu kuchokera m'buku la Genesis kufikira Chivumbulutso. Dongsosolo la Mulungu kwa Maiko amene kuchokera

poyambirira pa nthawi ziripo mwa tsatanetsatane. Zofunika panopa za moyo wa uzimu zinaperekedwanso. (ISBN #1-9030703-11-2).

**LUSO LOPHUNZITSIRA**

Phunziloli limawunika njira zimene Yesu anagwiritsa ntchito kulalikira uthenga. Ophunzira amaphunzitsidwa kuti angakonzekere komanso angapereke bwanji maphunziro ndikuti angaphunzitse ndi kulalikira bwanji uthenga wabwino. ISBN #1-9030703-12-0).

**NJIRA ZOFIKIRA ANTHU AMBIRI**:

Dongosolo la Mulungu lakufalitsira uthenga laperekedwanso. Phunziloli limawoneta kuti nkhristu m'modzi atha kukhala bwanji ndi udindo ofikira anthu mazanamazana a okhulupirila ophunzitsidwa komanso olimbikira. (ISBN #1-9030703-13-9)

**MPHAMVU YA MFUNDO:**

Mpingo oyamba unabadwa mwa chiwonetsero cha mphavu ya Mulungu. Mphavu ya fundo imene inga phunzitsidwe m'maphunzilowa ikonzekeretsa ophunzira ku khololа la uzimu ndikuwapanga kukhala owonetsa mphavu ya Mulungu osati owonerera chabe. (ISBN #19030703-14-7)

## BUKHU 4: KUIKA ZINTHU M'MALO
**Kuika m'malo zipangizo zobwera potsatira kuchulukitsa**

**MFUNDO ZA KAYENDETSEDWE KA ZINTHU MOGWIRIZANA NDI BAIBULO:**

Kawuniwuni wa mfundo za m'Baibulo zokhudzana ndi kulongosola zinthu zimene zima tsindika pa utsogoleri wopereka chitsanzo, utsogoleri wa m'Baibulo, dongosolo la m'mau a Mulungu zopambanira. (ISBN #1-9030703-15-5)

**MFUNDO ZA KAWUNIWUNI WA MALO OZINGULIRA:**

Ophunzira amaphunzira kawuniwuni wa malo ozungulira pokhazikika pa munthu, mpingo ndi bungwe. Amphunzira kuti angawunike bwanji malo ozungulira awuzimu monga mudzi, mzinda, chigawo cha dziko ndi dziko asanafike ndi uthenga wabwino. (ISBN #1-9030703-16-3)

**KAYENDETSEDWE KA ZINTHU MOLINGANA NDI ZOLINGA:**

Chilichonse chimene Yesu Khristu anapanga chinalunjika pa zolinga za Mulungu. Phunziloli limawunika zolinga za Yesu Khristu pa utumiki ndikuphunzitsa ophunzira nkhani ya kuyang'anira zinthu potsatira zolinga pa moyo wawo ndi utumiki wawo. ((ISBN #1-903070317-1)

## BUKHU 5: NJIRA ZOBWERETSA ZINTHU PAMODZI:

Kubweretsa pamodzi gulu la uzimu loyendetsa zinthu pogwiritsa ntchito zokumana nazo.

**NJIRA ZOBWERETSA ZINTHU PAMODZI:**

Phunziloli liwonetsa njira yobweretsa mphamvu za uzimu za Mulungu pamodzi ndi kufotokozera kagwiritsidwe ka zinthu ka masophenya a Harvestime ka magawo ena a utumiki. Maphunziro owonjezera alipo okhudzana ndi mbali zina za utumiki aperekedwanso kudzera m'mabuku ena. ISBN #1-9030703-18-x)

## BUKU 6: KUFALITSA

Masomphenya akukwaniritsidwa kudzera mdongosolo la utumiki wofanana ndi chotupitsa nkate.

**KUFALITSA UTHENGA MONGA CHOTUPITSA MKATE**

Uthenga wabwino unafalikira padziko lonse lapansi ngati chotupitsa mu ntanda wa nkate. Chotupitsa ndi chaching'ono komanso chimakhala chobisika koma mphavu yake ndiyopanda malire. Njira yofalitsira uthenga yabwino zaphunzitsidwa monga malangizo a utumiki wa utumiki wa mamasulidwe, kudzala mpingo, komanso luso la kulumikizana kwa mautumiki. (ISBN #1-9030703-19-8).

## *MAPHUNZIRO OWONJEZERA*

**AMAI, MANENEDWE A BAIBULO:**

Kuwerenga mabuku onse kumaphunzitsa za azimayi ndi ntchito yawo mutumiki. Zimakhudzananso ndi kuwerenga mabuku a m'Baibulo amene ali ndi maina azimayi monga Rute ndi Estere ndi malo amene mbiri ya azimayiwa imapezeka. (ISBN #1-9030703-20-1)

**UNABWERA KWA INE…BUKU LA UTUMIKI KUNDENDE**

Kalozera wokwanira wa utumiki wa pakati pa ansinga. Uli ndi mfundo zofunika kuzitsata potumikira pakati pa ansinga, komanso kutumikira kwa iwo amene ali pafupi kufa. (ISBN #1-9030703-22-8)

**PEMPHERO LOPEMBEDZERA:**

Pemphero lopembedzera ndi mfundo zotsogolera kuti mungapemphere bwanji, choyenera kupembedzera, mukuyenera kupembedzera chani, nthawi yoyenera kupembedzera, zoyenera kupembedzera, mapemphero adziko lonse, ndi zinthu zimene zimapangitsa kuti mapemphero abisike. (ISBN #1-9030703-23-6)

**NKHONDO YA THUPI:**

Kuwerenga mabuku onse amene amaphunzitsa za machiritso. Kalozera wokwanira, wa kulandira ndi kutumikira machiritso. (ISBN#1-9030703-21-x)

**CHOYENERA KUCHITA PAMENE SUKUDZIWA CHOYENERA KUCHITA:**
Kupezeka ngati uthenga wa pa tsamba la intaneti. Mokhazikika pa nkhani ya Jehosophat, bukuli limapereka dongosolo lakuti mukuyera kuchita chani nthawi ya mavuto pamene simukudziwa choyenera kuchita.

**KALOZERA WA GUWA LA UPANGIRI:**
Zimapezeka ngati uthnga ofufuzidwa pa tsamba la intaneti. Buku lophunzitsira atumiki a pa guwa.

**MFUNDO ZOMANGILIRA MABUKU A M'BAIBULO:**
Zopezeka pa tsamba la intaneti pokha. Mfundo zomagirira mabuku a m'Baibulo ndi mafuso otsogolera kuphunzira pa mapeto a Chaputala chilichonse.
**Mamphunziro owonjezera alipo pa tsamba la intanet:**
http://www.harvestime.org

**GAWO: 2**

## KALOZERA OTHANDIZA MUNTHU KUWERENGA MAU A MULUNGU

## KAYALIDWE A MAPHUNZIRO

Phunziro lirironse linalembedwa m'mabuku ogwirira ntchito. Ndichilolezo buku lirilonse litha kutengedwa pa tsamba la intérnate ndi kukasindikizidwa ndikugwiritsidwa ntchito pophunzitsa anthu ena. Malangizo a izi apatsidwa mgawo la kayang'aniridwe ka zinthu m'kalozelayi. Ophunzira atha kuphunzira za zipangizozi pa makina a komputa, ndi foni a m'manja.

Phunziro lilironse liri ndi:

**Tsamba la mau oyamba:** Phunziro limafotokozedwa ngati mbali imodzi ya Institute.

**Kagwiritsidwe ntchito ka kalozerayu**: Kalozera otsogolera kugwiritsa ntchito maphunzirowa.

**Malangizo pa kuphunzira mau pa gulu:** Mfundo zotsogolera kagwiritsidwe ntchito ka mpunziroli m'magulu.

**Mau oyamba a phunziroli:** Kuwonetsa bukuli limene ndi mbali imodzi ya phunziroli, kupereka dzina kwa phunziro ndi kuwonetsa chiyambi cha nkhani.

**Zolinga za Maphunziro:** Zolinga zambiri zanenedwa kumbali yakuti ophunzira ayenera kuchita chani akamaliza maphunzirowa.

**Kaikidwe ka zinthu m'chaputala:** Chaputala chirichonse chiri ndi mau oyamba, komanso ndandanda wa zolinga za chaputalacho. Ndime yotsogolera yoima pa mfundo zikuluzikulu zophunzitsidwa m'chaputalacho.

Zankati mwa phunziro zaperekedwa polemba mfundo zomangirira. Izi zitanthawuza kuti buku limagawidwa ndi mitu yaikulu, mitu yaing'ono, mitu yapadera imene imawonetsa za nkati mwa ndime zotsatira. Mayalidwe awa amapangitsa kuti ophunzira amphunzitse zimene waphunzira kwa ena potsatira mfundo zomangirira.

**Mafuso odziyesa:** Pamapeto pa chaputala chirichonse mayeso odziyesa nokha pamapeto pa buku. (Dziwani: Ngati mukuphunzitsa pa zochitika za pagulu ndipo simukufuna kuti ophunzira kuti akhale ndi mayankho, mukuyenera kuchotsa mayankhowa mukamasindikiza zipangizozi)

**Kudziwa zambiri:** Iri ndi gawo lomalizira m'chaputalachi. Limalilmbikitsa anthu kuwerenga pawonkha pa mutu opatsidwa.

## ZIPANGIZO ZOPHUNZIRIRA

Mndandanda wa maphunziro a ku Harvestime Institute anapangidwa mwa kuti mabuku ena samafunika kwenikweni kuti mumalizitse maphunziro onse. Sipafunika mabuku ena othandiza kuvetsetsa Baibulo monga Konkodansi, Atilasi, handbuku, ndi ena. Ngati muli ndi kuthekera kopeza mabukuwa mukulimbikitsidwa kuwagwiritsa ntchito koma sikuti opanda mabukuwa munthu sangamalize maphunziro. Mukungoyenera kukhala ndi Baibulo la King James m'chilankhulo chanu.

## NDONDOMEKO ZISANU NDI ZIWIRI ZOPHUNZIRIRA

Khazikitsani nthawi yapadera yowerenga tsiku lina lirilonse. Thawi zonse muziyamba ndi pemphero kwa Muungu kuti mzimu woyera alimbitse malingaliro anu kuti muphunzire chowonadi. Tsatirani "Dongosolo la ndondomeko 7"

### NDONDOMEKO YOYAMBA: Kafukufuku wa phunziro:

Werengani buku ndi mitu ya phunziro mgawo la mau oyamba mbuku limene mukugwiritsa ntchito. Gwiritsani ntchito ndandanda wa maphunziro opatsidwa mkalozerayi kuti muwone kumene maphunzilo akuyenera kukhala m'dongosolo la maphunziro a ku institute. Werengani mutu wa chaputala mgawo la "za nkatimu" la kalozerayi. Amapereka chithunzithunzi cha phunziloli. Werengani mau oyamba amene amawonetsa mutu wa phunziro. Werengani "zolinga za phunziro." Izi ndi zolinga zenizeni za kuphunzira phunzilo. Gwiritsani ntchito chaputalachi ndi ma chaputala ena onse gwiritsani ntchito ndondomeko yachiwiri kulekeza ya 6.

### NDONDOMEKO YA CHIWIRI: Kafukufuku wa chaputala:

Werengani "zolinga" za chaputala. Awa ndi masophenya amene mukuyenera kukwaniritsa pophunzira phunziroli. Werengani "Vesi lotsogolera" ndipo sungani pantima chifukwa cha mafuso "odziyesa nokha." Vesi imeneyi imamangirira ganizo lenileni m'chaputala. Werengani "Mau oyamba" m'chaputala. Mauwa amawonetsa zankati mwa phunziro. Werengani mwachidule chaputalachi, ndipo werengani mitu (mitu yokhazikia) ndi mitu yaing'ono (mitu imene iri chakumazere kumapeto kwa tsamba). Izi zimawonetsa mfundo zomangirira chaputala.

### NDONDOMEKO YA CHITATU: Kuphunzira chaputala

Panopa muli okonzeka kuphunzira chaputala mwandondomeko. Werenganiso chaputala chonse. Musasiye chilichonse. Mukamawerenga, tsekani mzere kunsi kwa mfundo zofunika ndipo lembani mafunso kapena mfundo zokuthandizani gawo lakumapeto kwa tsamba. Mukawuzidwa kuti muyang'ane ndikuwerenga malo ena m'baibulo, khalani otsimikizika kupanga choncho.

### NDONDOMEKO YACHINAYI: Kauniuni wa chaputala:

Unikani zolinga kumayambiriro kwa chaputala. Kodi mwakwaniritsa cholinga chirichonse pamene mumaphunzira? Ngati iyayi, werenganinso. Mutha kunenena vesi lotsogolera pantima?

Wunikani mitu yaikulu ya chaputala, mitu yaing'ono ya achaputala, ndi zimene mumalemba ndi zimene zinalembedwa mzere kusi.

**NDONDOMEKO YA CHISANU: Kudziyesa nokha:**

Yankhani mafunso odzifunsa nokha m'chapatala. Mukamaliza, fananitsani mayankho anu ndi mayakho anu ndi amene aperekedwa kumapeto kwa bukuli. Werenganinso kuti muwone ngati pali mfunso limene simunayankhe bwino.

**NDONDOMEKO YA CHISANU NDI CHIMODZI: Kudziwa zambiri:**

Pangani ntchito yopatsidwa m'gawo la kudziwa zambiri. Zochitika m'moyo watsiku ndi tsiku zikuthandizani kuti mudziwe kuphunzira panokha ndi kukulitsa chidziwitso chanu pa mutu umene mukuphunzira.

**NDONDOMEKO YA CHISANU NDI CHIWIRI: Kauniuni wa phunziro:**

Mukamaliza maphunziro onse m'chaputala, onaniso zolinga zazikulu zimene zapatsidwa kumayambiriro kwa bukuli. Kodi mwakwaniritsa zolinga zikuluzikulu? Ngati ayi, muyenera kuwunikanso magawo ena a phunziro lanu.

Mukamaliza phunziro, mkawundula wa ophunzira sungani tsiku limene mwamalizira. Kawundula wa ophunzira anaperekedwa mkalozerayi. Izi zikuthanizani kusunga maphunziro amene mwaphunzira.

## KUPHUNZIRA PA NGONGOLE

Ngati mukufuna kudziwa zambiri za kuti mungalandire bwanji ngongole ya Harvestime Institute, onani pafupipafupi Mafunso Ofunsidwa pa tsamba lathu la intaneti: http://www.harvestime.org

**HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE**
**KAUNDULA WA OPHUNZIRA**
**(Gwiritani ntchito fomuyi kusunga maphunziro amene mwamaliza)**

| BUKU | TSIKU MUNAMALIZA | MAPHUNZIRO |
|---|---|---|
| **KUPANGA MASOMPHENYA** | // | Njira zogwirira ntchito mkholola la uzimu. |
| **KUKHALA WOTSATIRA** | // | Maziko a chikhulupiro<br>Makhalidwe a mufumu wa Mulungu.<br>Ndondomeko za uzimu: Buku la nkhondo ya uzimu<br>Utumiki wa mzimu woyera<br>Kuzindikira liwu la Mulungu.<br>Njira zowerengera mau a Mulungu.<br>Kafukufuku wa m'Baibulo (Gawo 1 ndi 2) |
| **KUCHURUKITSA** | // | Kupanga mawonedwe a zinthu a wuzimu monga mwa mau Baibulo.<br>Njira zophunzitsira,<br>Njira zochulukitsira<br>Mphavu ya mfundo |
| KUIKA ZINTHU M'MALO | // | Mfundo zolongosolera zinthu<br>Mfundo zopangira kawuniwuni wa malo ozungulira<br>Kusamalira zinthu potsatira zolinga |
| KUBWERETSA ZINTHU PAMODZI | // | Njira zobweretsera zinthu pamodzi. |
| KUFALITSA UTHENGA | // | Kufalitsa kofanizidwa ndi chotupitsa mkate |

**GAWO 3:**

## KALOZERA WA KAYANG'ANIRIDWE KA ZINTHU

Gawoli limapereka ndonomeko zogwiritsira ntchto zipangizo za Harvetime Institute m'magulu.

## NTCHITO: KUPHUNZITSA ANTHU WAMBA:

Uthenga wabwino ukuyenera kulalikidwa kwa anthu onse. Kodi zikhoza kuchitika mu mbadyo uno. Pokhapokhapo ngati anthu wamba aphunzitsidwa kufalitsa uthenga wabwino. Tikamati anthu wamba tikuthanthawuza amuna kapena azimayi amene satumiki. Amenewa ndi anthu ambiri mu mpingo. Kusiyana ndi kusiyanitsa pakati pa azibusa ndi anthu wamba, tikuyenera kuthandiza aliyense amene anabadwa mwatsopano kuzindikira ntchito yake angati munthu pokwaniritsa ntchito imene anatisiyira. Dziko lapansi silingafikilike ndi uthenga wabwino ngati ntumiki amazindikira ntchito yawo yolalilkira uthenga. Sikuli azibusa ophunzitsika bwino kuti ntchito igwirike.

Kugwiritsanzo ntchito anthu wamba kunali ngati mfungulo wa kukula kwa m'pingo. (Machidwe 8:1) timawerenga kuti chinzuzo cha a khristu chinadzetsa chibalaliko padziko lonse lapansi ku Samaliya ndi atsgoleri a mpingo anatsalira ku Yerusalemu ndipo timapeza kuti..

> **Pamenepo ndipo iwo akubalalikitsidwa anapitiapita nalikira mauwo. (Machitidwe 8:4)**

Osati atsogoleri okha komanso anthu wamba amene amalalilkira anakwaniritsa ntchito yaikulu pofalitsa uthenga wabwino.

Kuchokera pachiyambi, kufalitsidwa kwa utheng kunatsogoleredwa ndi anthu wamba. Anthu ngati Yonane ndi Petro anali asodzi osaphunzira. Ntchito yambiri ya utumiki ndi zochitika chitika mumpingo oyambirira inakwaniritsidwa ndi anthu amene sanali akatswiri, anthu amene amagwira ntchito zina tsiku ndi tsiku.

Pamene Sauli amafuna kuwononga mpingo wonse. Baibulo limati analowa mkachisi ndi myumba iriyonse kugwira okhulupirira kuti akhale akapolo (Machitidwe 8:3). Anazindikira kuti kuletsa mpingo ndi atumiki sikungaletse kufalitsidwa kwa uthenga wabwino. Munthu wamba aliyense anali wakubala zipatso ndipo khomo lina lirilonse linali malo akufalitsa uthenga wabwino.

Ngati tikufuna kufikira dziko lapansi ndi uthenga wabwino ndi kuti daniyo asapite patsogolo, azibusa ndi anthu wamba akuyenera kugwirana manja. Okhulupirira sikuti ndi zidutswa chabe za mpingo zofalikira mdera lonse amene amabwera pamodzi kulambira, kulandira malangizo ndi chiyanjano cha akhristu. M'magwiridwe awo a ntchito, komanso m'makhalidwe ali oyimira ufumu wa Mulungu amene atha kufikira athu amene sangalowe ku tchalitchi kapena kulowa munsokhano wa Uzimu.

Paulo anamuwuza Timoteo kuti asankhe anthu okhulupirika ndikuwaphunzitsa zinthu zimene iye anaphunzitsidwa. Anthu okhulupirikawa amayenera kukhala ndi kuthekera kophunzitsa ena.

Kudzera ku dongosolo lokhazikika lophunzitsira anthu wamba, uthenga wabwino ungafalikire padziko lonse lapansi.

Ndimasankhidwe “Amuna kapena akazi” okhulupirika amene ndi makiyi a utumiki wabwino akuphunzitsa anthu wamba. Dziko lapansi limatenga anthu aluso ndikuyesera kuwapatsa khalidwe. Amakhazikika pa kupanga anthu kukhala akatswiri. Mulungu anati “tengani anthu okhulupirika” akhalidwe labwino ndipo iye adzawapatsa mphavu ndi kuthekera kwa uzimu komanso luso.

Potsatira dongosolo lopatsidwa pa 2 Timoteo 2:2, mpingo utha kukula wodabwitsa ngakhale kuyang’ana pa utumiki wa munthu pa munthu makulidwe ake ndi odabwitsa.

Onani tchati pa tsamba lotsatira. Chikugwiritsa ntchto nthawi pa chaka ngati mulingo wabwino wa kuchuluka kwa nthawi yofunika kuphunzitsa munthu wobadwa kumene mwatsopano ndikumpanga kuti akhale ndi kuthekera kobereka zipatso. Koma ndondomekoyi itha kutenga nthawi yochulukirapo kapena yocheperapo potengera kuchuluka kwa anthu amene akukhudzidwa.

Koma kutenga chaka ngati mulingo wabwino, ngati okhulupirira angafikire munthu m’modzi ndikumuphunzitsa chaka chirichonse ndikuwapanga kuti alonjeze kuphunzitsa munthu m’modzi chaka chilichonse, dziko likhoza kufikiridwa mosavuta ndi uthenga wabwino.

Onani pa tchati kuti m’chaka choyamba okhulupirira akuphunzitsa munthu m’modzi. Ku mapeto kwa chaka chachiwiri, kuli anthu okwanira anayi, aliyense wa awa adzaphunzitsa munthu m’modzi chaka chotsatirachi.

| | **Mphunzitsi** | **Ophunzira** | | **ONSE** |
|---|---|---|---|---|
| Chaka 17 | 65, 536 | 65,536 | = | 131,072 |
| Chaka 16 | 32, 768 | 32,768 | = | 65,536 |
| Chaka 15 | 16, 384 | 16,384 | = | 32,768 |
| Chaka 14 | 8, 192 | 8,192 | = | 16,384 |
| Chaka 13 | 4, 096 | 4,096 | = | 8,192 |
| Chaka 12 | 2, 048 | 2,048 | = | 4,096 |
| Chaka 11 | 1, 024 | 1,024 | = | 2,048 |
| Chaka 10 | 512 | 512 | = | 1,024 |
| Chaka 9 | 256 | 256 | = | 512 |
| Chaka 8 | 128 | 128 | = | 256 |
| Chaka 7 | 64 | 64 | = | 128 |
| Chaka 6 | 32 | 32 | = | 64 |
| Chaka 5 | 16 | 16 | = | 32 |
| Chaka 4 | 8 | 8 | = | 16 |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| Chaka 3 | 4 | 4 | = | 8 |
| Chaka 2 | 2 | 2 | = | 4 |
| Chaka 1 | 1 | 1 | = | 2 |

**DONGOSOLO LA MULUNGU PA KURUKITSA NDI KUBWERETSA ZINTHU PAMODZI**

Mukatenga mpingo umene ma membala ake ndi pafupifupi 100 ndikuti mukulitse chati kufikira anthu 100, aliyese kuphunzitsa munthu wina chaka chirichonse ndikuti ophunzira amenewa amayamba kuchuluka, ndipo ndichapafupi kuwona kuti tingafikire bwanji dziko lonse lapansi m'badyo wathu.

Yesu anadalira anthu wamba ndi udindo waukulu wa uthenga wabwino. Kutenga asodzi kuti asiye ngalawa zao, anawapanga kukhala asodzi awanthu. Anakhulupirira kuti anthu wamba antha kukhala odabwitsa akapatsidwa mphavu ndi mzimu woyera.

Cholinga cha Harvestime International Institute ndi kufalitsa masophenya ophunzitsa anthu wamba imene iri njira ya Mulungu yopulumutsira anthu ambiri padziko lonse lapansi. Ndi anthu wamba amene Institute yakonzeka kugwiritsa ntchito ngati njira yobalira zipatso ya 2 Timoteo 2:2 imene tinadzipereka.

**MALUSO OMUYENEREZA MUNTHU**

Kudziwa kuwerenga ndi chofunika kwa ophunzira kuti agwiritse ntchito zipangizo pawokha.

**KUPANGA ZIPANGIZO KUFANANA NDI ANTHU OSAPHUNZIRA**

Ngati gulu kapena ma membala onse lalephera kufikira pa mulingo wokhala ndi luso lowerenga, mfundo zotsogolera zopanga zida kusinthika ndikufanana ndi anthu osaphunzira zaperekedwa ndi Harvstime Institute mutu wake "Luso lakuphunzitsa."

**KUKHAZIKITSA MASUKULU OKHAZIKIKA**

Malangizo okhazikitsira Harvestime International Insitute aperekekedwa m'phunziro limene mutu wake ndi "Njira zochulukitsira." Timaperekanso uthenga pa intenate wa zonse zimene zingafunike kuti muyambitse maphunziro mdera lanu. Ndondomeko yokwanira, fomu, kaundula, mayeso aphunziro handbuku ndi zina. Onani gawo la ongoyamba kumene pa tsamba lanthu la intaneti.

**KASUNGIDWE KA KAUNDULA WA ZINTHU**

Ngati mukuphunzitsa maphunziro onse ndipo mukufuna ophunzira kuti alandire pepala losonyeza kuti amaliza maphunziro, pangani ma buku a "kaundula wa ophunzira", fomu pa gawo lachiwiri la kalozelayi. Sungani kaundula wa ophunzira aliyense kapena khalanindi ophunzira amene akusunga okha kaundulayi. Mukamaliza maphunziro onse monga mwa ndandanda wa buku la ophunzira, mutha kupanga pepala la umboni mdela lanu ndikupereka kwa ophunzira.

## KUPHUNZIRA M'MAGULU: KUKONZEKERERATU

Ngati simunaphunzitsepo pagulu, tikuganiza kuti muphunzire phunziro pa sukuluyi otchedwa "Luso lophunzitsira." Phunziloli limayima kwambiri pa njira zimene Yesu Khrustu anagwiritsa ntchito pophunzitsa akuphunzira amene anafikira dziko lonse ndi uthenga wabwino. Tsatirani ndondomeko zimenezi kuti muyambitse sukuluyi:

1. Itanitsani kapena fufuzani pa tsamba la interneti la Harvestime International Insitutue phunziro loyamba limene mwapanga dongosolo kuti kuphunzitsa.
2. Malizani pempho lopanga mapepala ena ndipo sindikizani ma pepala okwana a phunziro la gulu lanu.
3. Ngati mukuphunzitsa ndandanda onse wa maphunzirowa, sindikizani fomu ya "Kaundula wa Ophunzira" kuti musunge uthenga wokhudzana ndi m'mene maphunziro awo akuyendera. (Onani mbali yachiwiri ya kalozera).
4. Itanani pamodzi gulu la okhulupirira okhudzika kuti muthanizane kupempherera, kuika zinthu m'malo, ndikulengeza za maphunzirowa.
5. Khazikitsani donsosolo la bungwe. Pezani atsogoleri, aphunzitsi, ndi maudindo awo. Ikani nthawi, masiku, ndi malo opangila maphunziro.
6. Lengezani za sukuluyi: Ngati mwasankha atsogoleri ndipo maphunziro Sali a anthu wamba onse, simufunika kuti mulengeze za sukulu yanu. Dziwitsani aliyense wa Atsogoleri ndipo apatseni nthawi, tsiku, ndi malo a maphunziro oyamba. Ngati maphunziro ndiovomerezeka kwa anthu onse a mdela lanu mukuyenera kulengezetsa nthawi ya msonkhano wanu.

   Ngati mumakhala madera akumudzi kapena ovuta kufikirika mutha kudziwitsa anthu pogwiritsa ntchito mau a pakamwa panu. Ngati mumakhala mu'mzinda, mutha kusindikiza mapepala authenga kuti mukagawe. Ikani mapepalawa pali ponse pamene Akhristu amakumana. Ikani m'tchalitchi, zipinda zosungila mabuku, ndipo funsaninso abusa pampingo wa mdela lanu kuti alengeze za maphunzirowa kuchokera pagome kapena mapepala a amauthenga.

   Pezani mdandanda wa manambala otumimizira makalata a mabungwe ndi ma tchalitchi osiyanasiyana ndipo tumizani zolengeza zanu kudzera posoti ofesi ngati izi ziripo mdera lanu. Tumizani zolengeza zanu za Insitute ku wailesi wailesi yakanema ndi bungwe losindikiza nkhani mdela lanu.

   Pa zolengeza zonse, ikani dzina la bungwe lanu, tsiku, nthawi, ndi malo ndi cholinga cha msonkhano wanu. Kuwonjezerapo dzina lanu, adiresi, ndi namabala ya foni imene anthu atha kugwiritsa ntchito ngati angakhale ndi mafuso ambiri.

   *Harvestime iri ndi uthenga wambiri umene ukhoza kukuthandizani ku khazikitsa sukulu pa magazini yotchedwa "Institute Yoyamba kumene". Ngati mumakhala kunja kwa US: Mutha kupempha magazini yaulele koma yotumizidwa kudzera pa makina a intaneti.*

*Ngati mumakhala ku US, mutha kuitanitsa magazini kuchokera mzipinda zogulitsira mabuku kapena tsamba la intaneti;* ***http://www.harvestime.org***

## KUPHUNZIRA KWA PAGULU: KUPANGITSA MAPHUNZIRO

**MSONKHANO OYAMBA:**

-Yambani nsokhano oyamba ndi pephero kenako mwambo odziwana.
-Tengani maina ndi adiresi ya aliyense amene wabwera. Izi zikulolezani kulumikizana nawo nthawi ya nsokhano wina isanakwane.
-Fotokozani dongosolo la gulu: Atsogoleri, amphunzitsi, masiku, nthawi ndi malo amene msonkhano uzichitikira.
-Khalani ndi nthawi ya kulumbira ndi kuyamika Mulungu, kuitana kupezeka kwa Mzimu woyera pa maphunziro anu.
-Dziwitsani koyamba za Harvstime Intenartional Insitutue ndi zolinga ndi masophenya ake. Gwiritsani ntchito zipangizo zopatsidwa m'gawo loyamba la kalozera.
-Onetsani chithunzithunzi cha ndandanda wa maphunziro onse ngati mungagwiritse ntchito maphunziro onse. Fotokozani kugwirizana kwa phunziro loyamba m'maphunziro onse. -Perekani ma buku aphunziro loyamba.
-Pangani kawuniwuni ndi ophunizira wa "ndondomeko 7 zophunzirira" zothandiza kuphunzira pawekha zimene zinapatsidwa m'gawo lachiwiri mbuku la kalozera. Perekani kwa ophunzira aliyense pepala la ndondomekozi kuti zitsogolele akamaphunzira paokha. Nthawi iriyonse mwayamba phunziro latsopano, onani kafukufuku wa phunziro ndi ophunzira (ndondomeko yoyamba ya "ndondomeko 7" zimene zinapatsidwa m'gawo lachiwiri mkalozerayi)
-Onetsani chithunzithunzi cha phunziro loyamba. Perekani ntchito kuti ophunzira awerenge ndi kumalizitsa tsiku la nsokhano wachiwiri lisanafike. -Malizani nsokhano ndi pephero ndi kutumikira ophunzira.

**MISONKHANO YOTSATIRA:**

-Yambani ndi pephero.
-Landirani ophunzira oyamba kumene ndipo apatseni mabuku ophunzirira.
-Kuyamika ndi kulambira.
-Phunziro: Kambirananai gawo lirironse la chaputala limene ophunzira awerenga. Fusani ngati ophunzira lai ndi mafunso kapena ndemanaga.
-Unikani "mafunso odziyesa nokha" pamodzi. Onani m'mene ophunzira anachitira pa mayesowa. Mutha kufuna ku onanso gawo la "Kuphunzira Zambiri" ngati gulu kapena ngati munthu.

-Gawanani zonse zimene munaphunzira zowonjezera pa mutuwu. Gwiritsani ntchito njira zosiyanasiyana zophunzitsira.

-Fusani mafunso
-Pangitsani kukambirana kwa m'magulu
-Gwiritsani ntchito tchati ndi zojambula pofotokozera phunziro lanu.
-Ophunzira awonetse ma repoti a magawo ena a phunziro.
-Ophunzira ayenera kutanganidwa, machitachita ndi njira yabwino yophunzirira. -Gwiritsani ntchito phunziro ku moyo wa ophunzira. Tsindikani pa zochitika za moyo watsiku ndi tsiku, machitachita ndi chiwonetsero.

-Perekani nthawi yapadera yakuti anthu akhoza kudziperekanso mwapadera kwa Mulungu.
-Tumikirani amene ali ndi zofuna zapadera ndipo lolani Mzimu Woyera kuyenda nthawi imene mukuphunzitsa.

**KUMALIZITSA PHUNZIRO:**

-Osayiwala kumalizitsa ma fomu a "Mkawundula wa Ophunzira" ngati gulu lanu likufuna kukhala ndi makalata osonyeza kuti munamaliza maphunziro. Mukhale ndi mwambo opereka ma setifiketi amene akuyenera kusindikizidwa mdela lanu. Limbikitsani ophunizira kugwiritsa ntchito zimene aphunzira ndi kuphunzitsa ena chaka chotsatira chisanathe. Izi zithandiza kukulitsa ndi kulumikizana kwa maphunzirowa.

Ngati ophunzira akuwonetsa chidwi pophunzitsa pagulu:

1. Mupatseni buku la "Maphunziro oyamba ndi kalozera wa kuyang'anira"
2. Muwonetseni gawo la "Maganizo a Kuphunzira kwa pa Gulu" limene linaperekedwa m'mabuku a maphunizrowa.
3. Mupangireni kuti achite nao maphunziro a "Luso la Kuphunzitsa"

## HARVESTIME INTERNATIONAL NETWORK

### Malamulo a Kumasulira ndi Kusindikiza Mabuku

Tavomereza udindo wa pa Habakuku 2:2 ndi Masalimo 68:11. Ambuye anatiwuza kuti "Lemba masophenya ndipo muwachanutse" koma tiyenera kuwapititsa kwa amene angathamange nawo. Awa ndiwo amene akufalitsa uthenga. Ndichifukwa chake timalola kumasulira ndi kusindikiza mabuku ambiri potsatira malamulo awa. Harvestime Institute imapereka mwayi omasulira ndi kusindikiza mabukuwa potsatira mfundo izi:

1. Kusasinthidwa kwa mfundo zolembedwa pokhapokha ngati ziri zoyenera makamaka mamasulidwe akamachitika kuchokera ku chilankhulo china kupita kuchilankhulo china.
2. Tsamba loyambirira, lomaliza ndi masamba amau oyamba sakuyenera kusinthidwa, omalizidwa ndi adiresi yathu. Masamba amenewa amawonetsa zipangizo zololezedwa ndi bungwe lanthu ngati pakufunika mabuku owonjezera.
3. Kusindikiza mabuku ndikovomerezeka koma osati kuti akagulitsidwe. Mabuku abwino akhoza kugulidwa ku Harvestime Time. Iyi ndi njira imodzi imene timathandizira bungweli kuti tizipereka zinthu kwa ulele pa tsamba la intaneti komanso kunja kwa dziko la Amerika.
4. Buku limene mwasindikiza silikuyenera kugulitsidwa pantengo odutsa 15% ya zonse zimene munagwiritsa ntchito kuti musindikize. Ntengowu ndiwokwanira kuti mubweze ndalama imene munagwiritsa ntchito kuti musindikize mabuku ena. Tinaika malile amenewa a 15% pamwamba pa zonse zimene munagwiritsa ntchito kuti zipangizozi zisagwiritsidwe ntchito popanga phindu kapena kuti mitengo isakwere kwambiri kufikira kuti anthu wamba sangakwanitse. Muli ndi ufulu ogulitsa mabuku anu pantengo okwanira ndalama zimene munagwiritsa ntchito kapena mukhoza kungopereka ngati chuma chingakulololeni kutero.
5. Fomu ya " Chidziwitso chosindikizira" kapena chidziwitso chomasulira" iperekedwe ndi kuvomerezedwa ndi Harvestime International Network"
6. Ngati mukumasulira phunziro, buku lomalizira limene mwa masulira litumizidwe ku Harvestime International Network.
7. Malamulo a intaneti: Muli ololedwa kutenga maphunzilowa kwa ulele ndikuwaika m'makina anu a komputa, kusindikiza mabuku ambiri. Muthaso kupita pa tsamba lathu la intaneti kapena kuika maphunzirowa pa tsamba lanu ndi linki ya tsamba la intaneti ya Harvestime. Maphunziro ochitika pa tsamba la intaneti siwolipitsa. Ngati anthu akufuna kuphunzira chifukwa cha malikisi akuyenera kulembetsa pa tsamba la intaneti la Harvestime. Tsamba lathu ndi http://www.harvestime.org

Tinavomereza udindo wa pa Habakuku 2:2 ndi Masalimo 68:11. Ambuye anatiwuza kuti "lemba masophenya ndipo uwachanutse." Koma tikuyenera kuwasiya m'manja mwa amene angathamange nawo, amene amalalikira. Ichi ndi chifukwa chake timalola kuti mabukuwa atha kusindikizidwa ambiri ndi kumasulilidwa mziyankhulo potsatira malamulowa.

## HARVESTIME INTERNATIONAL NETWORK

### Chidziwitso Chosindikizira Mabuku ena Ambiri

Dzina lanu: ______________________________

Adiresi: ______________________________

Dzina kapena bungwe limene mukuyimira: ______________________________

Mudzagwiritsa ntchito zida zimene mupange: ______________________________

Harvestime International Network imasunga chilolezo chosindikizanso ndandanda wa mabuku okonzedwa ndi Insitute koma imapereka mwayi ochulukitsa mabuku potsatira mfundo izi:

1. Sipapezeka kusintha kwina kulikonse mzipangizo koma zokhazo zoyenera ndipo zokhudzana ndi chilankhulo ngati nkhani ikumasulidwa mchilankhulo china.
2. Chikuto ndi masamba oyambirira amasungidwa ndi kuchulukitsidwa.
3. Buku silimagulitsidwa pantengo odutsa 15 % ya zonse zimene munazigwiritsa ntchito popanga bululo
4. Fomu ya chidziwitso chopangira mabuku ena imalizidwe ndi Harvestime International Network.

Ndikuvomera kukhanzikika pa malamulo amenewa:

Siginecha________________________________Tsiku___________________

**Tumizani pepho lanu limene mwamaliza ku likulu la Harvestime International** 3176 A Via Buena Vista, Laguna Woods, CA 92637, USA.

**HARVESTIME INTERNATIONAL NETWORK**

**Chidziwitso Chomasulira**

Dzina Lanu: ___________________________________________________________________

Adiresi: ___________________________________________________________________

Dzina la mpingo kapena bungwe mukuyimira_____________________________________________

Mukagwiritsa ntchito bwanji zipangizo zimene mukumasulira? ___________________________________________________________________

Ndimaphunziro ati amene mukufuna kumasulira?________________________________________

Kodi mumasulira mchilankhulo chanji?__________________________________

Harvestime International Network imasunga chilolezo chosindikizira ndandanda wa mabuku onse amene akonzedwa ndi Insitute koma imapereka mwayi potsatira mfundo izi:

5. Sipapezeka kusintha kwina kulikonse mzipangizo koma zokhazo zoyenera ndipo zokhudzana ndi chilankhulo ngati nkhani ikumasulidwa mchilankhulo china.
6. Chikuto ndi masamba oyambirira amasungidwa ndi kuchulukitsidwa.
7. Buku silimagulitsidwa pantengo odutsa 15 % ya zonse zimene munazigwiritsa ntchito popanga bululo
8. Fomu ya chidziwitso chopangira mabuku ena imalizidwe ndi Harvestime International Network.

Ndikuvomera kukhanzikika pa malamulo amenewa:

Posainira__________________________________Tsiku____________________

**Tumizani pepho lanu limene mwamaliza ku likulu la Harvestime International** 3176 A Via Buena Vista, Laguna Woods, CA 92637, USA.